

# MATENDA A TOXOPLASMOSIS

KUTSEKULA ZINSINI ZA TIZILOMBO TODABWITSA TOSAONEKA NDI MASO



University  
of Glasgow

Wellcome Centre  
for Integrative  
Parasitology



**MATENDA A TOXOPLASMOSIS= KUTSEKULA ZINSINSI ZA TIZILOMBO  
TODABWITSA TOSAONEKA NDI MASO NDI BUKU LA NTHABWALA LOMWE  
LINATSINDIKIZIDWA NDI WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY,  
A JAMIE HALL NDI A EDWARD ROSS MUCHAKA CHA 2022.**

BUKULI LINALEMBEDWA NDI A JAMIE HALL NDI A EDWARD ROSS. LINANTANHAUZIRIDWA  
MUZINTHUNZI NDI A EDWARD ROSS. DR LILACH SHEINER ANATHANDIZA NDI ULANGIZI WA  
SAYANSI.

ULAMULIRO WONSE WA BUKU LI NDI WA WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE  
PARASITOLOGY NDI OLEMBA. SIKOLOLEDWA KUTI GAWO LILILONSE LA BUKULI  
LITSINDIKIZIDWE KAPENA KUKOPEDWA MWANJIRA ILIYONSE POPANDA CHILOLEZO CHA  
OTSINDIKIZA NDI OLEMBA.

BUKULI LINASINDIKIZIDWA NDI WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY, SIR  
GRAEME DAVIES BUILDING, UNIVERSITY OF GLASGOW, 120 UNIVERSITY PLACE,  
GLASGOW G12 8TA

BUKULI LINA SINDIKIZIDWA PA MAPEPALA OBWEZEREDWANSO

KUSAKA KWAYAMBIKANO



KHOSWE UYU AKUONEKA NGATI KA CHAKUDYA  
KU MPHAKA AKUMUTHAMANGITSAYO

KOMA MKATI MWAKE MWAGONA  
TIZILOMBO TAMBIRI TOSAONEKA  
NDI MASO TOMWE TIKUFUNAFUNA  
THUPI LOTI TILOWEMO



MPHAKA WOPUSA, SUNAMVE  
CHILICHONSE CHIMENE  
NDIMAKUZA POMPANO?



MEW?



KHALA PANSI. NDUGANIZA NGATI NDI NTHAWI YOTI TICHEZE ZA MATENDA OTCHEDWA TOXOPLASMOSIS



AKA NDI KACHILOMBO KA TOXOPLASMA


NDI KACHILOMBO KOSAONEKA NDI MASO KAMENE NDIMAKHALA NDIKUKAPHUNZIRA TSIKU LIRILONSE KUNTCHITO



NDI KODABWITSA MU ZOTENGELEKA, KAMATHA KUFALA KWA NYAMA ZAMBIRI

MUCHILICHONSE KUYAMBIRA MVUU, A KADYANSONGA, NKHOSA, MAKOSWE NGAKHALE ANTHU

MEWZ! (said by the cat on the cow)



KOMABE, MALO AKE OKHALAMO NDI MKATI MWA THUPI LA AMPHAKA NDIPO KUFALIKA KWAKE KUMAKHALA KOBWERERABWERERA KUCHOKELA KWA AMPHAKA NDI NYAMA ZATSOKA ZOMWE ZIMASAKIDWA




KHOSWE AMENE UMATHAMANGITSA UJA... AKANAKHALA ALI NDI TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDA WA NDIPONSO UKANA MULUMA, NAWENSO UKANATENGA TIZILOMBO TI

TIZILOMBOTI TIKANATHA KUPEZA MALO OKHALAMO MMIMBA MWAKO, KENAKA KUCHULUKANA NDI KUFALA KU NYAMA ZINA. MWINANSO NDI INENSO

KACHILOMBO KA SIKAMAFALIKIRA POKHAPOKHA MWINI THUPI WOKHALA NDI TIZILOMBO TI WADYEDWA KAPENA KULUMIDWA. KALI NDI NJILA ZINA ZOMWE KAMAFALIKIRANSO



M'MIMBA MWA AMPHAKA, TIZILOMBO TI TIMAPANGA TINTHU TING'ONOTING'ONO TOLIMBA TOUNDANA NGATI CHOTUPA TOMWE TIMATULUKA KUDZERA M'CHIMBUDZI



NGATI MATCHELA, TIZILOMBO TOKHALA NGATI ZITUPAZI TIMAKHALA MU UBWEYA KAPENA MU CHILENGEDWE KWA ZAKA, NKUTULUTSA TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDA TIKAPEZA MWAYI OLOWA M'NYAMA ZINA

UKHOZA KUTENGA TIZILOMBO TI KUDZERA MU FUMBI LAKUDIMBA, MU UBWEYA WA NYAMA KAPENANSO POKUDYA ZAKUDYA ZOSAPHIKIDWA MOKWANIRA




KWA NTHAWI ZAMBIRI, TIZILOMBO TI SITOOPA KWAMBIRI KWA ANTHU. PAFUPIFUPI THEKA LA ANTHU ALI NDI TI ZILOMBO TI, NDIPO AMBIRI MWA IWO SAMADZIWA NDIKOMWE



KOMA NTHAWI ZINA, TIZILOMBO TI TIMATHA KUONONGA KWAMBIRI, POYAMBITSA MATENDA OTCHEDWA TOXOPLASMOSIS.

AZIMAYI OYEMBEKEZER A AKHOZA KUPATSIRA TIZILOMBO TI KWA ANA AWO OSABADWA, ZIMENE ZIMAKHALA ZOSAKHALA BWINO.



KOMANSO, NGATI CHITETezo CHA M'THUPI CHA MUNTHU CHAONONGEKA CHIFUKWA CHA MANKWALA KAPENA MATENDA ENA MONGA EDZI NDI KHANSA - TIZILOMBO TI TIMAKHALA TOOPA, KUONONGA UBONGO, MTIMA, MAPAPO KAPENANSO MASO.

NTCHITO YANGA NGATI KADAULO WAZA  
SAYANSI NDIYOFUNA KUMVETSETSA MMENE  
TIZILOMBO TI TIMAGWIRIRA NTCHITO  
KOMANSO CHIMENE CHIMAPANGITSA KUTI  
TIZIKHALA TOPAMBANA KWAMBIRI  
POYAMBITSA MATENDA

M'MENE  
TIKUPHUNZIRA  
ZAMBIRI ZA IZI,  
TIKUZINDIKIRA  
NDIKUONA  
ZAMBIRINSO  
ZODABWITSA ZA  
TIZILOMBO TI

MMENE UKUDZIWIRA, NJIRA IMODZI  
YOTI TIZILOMBO TI TIFALE NDIKUTI TIDYEDWE  
KAYE. TIMAFUNA NYAMA ZOMWE TILIMO  
ZO ZIDYEDWE.

KOMA PALI VUTO,  
MAKOSWE CHIBADWIRE  
CHAWO AMAOPA  
AMPHAKA KOMANSO  
FUNGO LA AMPHAKA  
LIMAWAPANGITSA  
KUKHALA ATCHERU



ZIKHOZA KUKHALA  
ZOTHANDIZA KWA  
TIZILOMBO TI NGATI  
KHOSWE ANALI  
WOSASAMALITSA NDI  
WOPANDA TCHERU

TIZILOMBO TI TIKAFIKA  
KU UBONGO, IZI  
NDIZIMENE  
ZIMACHITIKA



MAKOSWE AMENE ALI NDI TIZILOMBO  
TI AMAKHALA OPANDA TCHERU NDIPONSO  
AMAKHALA OKOPEKA NDI FUNGO LA AMPHAKA



KUKHALA  
CHAKUDYA  
CHOSAVUTA  
KUPEZA KWA A  
MPHAKA NDI  
KOOPSA KWA  
MAKOSWE, KOMA  
ZIKUONEKA NGATI  
IMAKHALA NJIRA  
YABWINO IMENE  
TIZILOMBO TI TIMA  
ZITHANDIZIRA  
KUFALA KWA  
AMPHAKA  
ENA



ZOTSATIRA ZA TIZILOMBO TI KU CHIKHALIDWE CHAMAKOSWE KWAPANGITSA A ZAKAFUKUFUKU KUTI AGANIZE ZOTI TIKHOZA KUSINTHANSO CHIKHALIDWE CHA MUNTHU

AZAKAFUKUFUKU AKUGANIZIRANSO NGATI TI ZILOMBO TI TITHA KUYAMBITSA MITUNDU INA YA MISALA KWA ANTHU KAPENANSO KUPANGITSA ANTHU KUTI AZIKHALA OSASAMALA ZIMENE ZINGAMAPANGITSE NGOZI ZA PA MSEWU NDI MACHITIDWE ENA OOPSA.



NDIZOOPSA KUTI TIZILOMBO TATING'ONO NGATI ITI TIKHOZA KUMATILAMULIRA

KOMA NZOSADZIWIKA NGATI TIZILOMBO TI TIMAKHUDZA CHIKHALIDWE CHA ANTHU



NGATI AKADAULO AZA SAYANSI, NDI NTCHITO YATHU KUFUNSA NDIKUYESA ZOMWE AKADAULO ENA AZA SAYANSI APEZA

CHIFUKWA CHA ICHI, AZAKAFUKUFUKU ENA AKUTSUTSANA ZA MGWIRIZANO WA PAKATI PA KUDWALA MATENDA A TOXOPLASMOSIS NDI MISALA KAPENA MCHITIDWE OSASAMALA



KUKUFUNIKA KAFUKUFUKU WAMBIRI. NDIZOTHEKA KUTI ZIFUKWA ZINA NDI ZIMENE ZIMAYAMBITSA MISALA YI KOMANSO KUTI TIZILOMBO TI SITIMAYAMBITSA MISALA YI KUMENE




NGAKHALE KUTI TIZILOMBO TI  
SITIKUTISANDUTSA KUKHALA AMISALA  
KAPENA OSASAMALA, NDI TIZILOMBO  
TODABWITSABE



KUNO KU  
WELCOME  
CENTRE FOR  
INTEGRATIVE  
PARASITOLOGY  
TILI PALIKILIKI  
KUFUFUZA  
CHIMENE  
CHIMAPANGITSA  
KACHINTHU  
KAKANG'ONOKA  
KOSAUTSAKA  
KAZITERE



NGAKHALE KALI KAKANG'ONO,  
KACHILOMBOKA SIKAMASEWERA



MONGA NGATI MAKINA OONERA  
TIZILOMBO TATING'ONOTING'ONO  
OTCHEDWA MICROSCOPE, TIZILOMBO  
TI TILI NDI TIZIDUTSWA  
TOSUNTHASUNTHA KOMANSO  
TIZINTHU TINA TOBISIKA

ZIMATHEKA BWANJI TIZIDUTSWA TI KUKHALIRA  
PAMODZI, KUMAYENDA, KULOWA MU TIZIGAWO  
TA M'THUPI MWATHU, KUCHULUKANA NDI  
KUPHULIKA KENAKO NDIKUFALIKIRA?



NJIRA IMODZI YOMWE TINGADZIWIRE IZI  
NDI KUGWIRIRA NTCHITO LIMODZI POFUNA  
KUDZIWA CHITHUNZITHUNZI CHENICHENI  
CHA TIZILOMBO TOVUTITSA TI



MWA MWAYI, TILI NDI ZIPANGIZO ZAMPHAVU ZOMWE TIMAGWIRITSA NTCHITO POONA ZOMWE ZIKUCHITIKA MKATI MWA TIZILOMBO TI



POTENGA MAJINI A NSOMBA ZA M'MADZI ZINA ZAKE ZOWALA, TIMATHA KU WA LUMIKIZA KU MAJINI A TIZILOMBO TI ZIMENE ZIMAPANGITSA KUTI TI ZIWALA NAONEKA BWINO PA MAKINA A MICROSCOPE. TIKATERO TIMATHA KUONA ZIWALO ZA TIZILOMBO TI NDI MMENE ZIMAGWIRIRA NTCHITO



NDIPO UPANGIRI WA ZA MAJINI UMATITHANDIZA KUTI TICHOTSE KAPENA KUSINTHA TIZIWALO TA TIZILOMBO TI KUTI TIZIWE ZIMENE TIZIWALO TI TIMACHITA



UPANGIRI WU UKUNKA NAPITA MTSOGOLO NTHAWI ZONSE. MBUYOMO, KUFUFUZA ZA JINI IMODZI KUMATENGA ZAKA ZAMBIRI



UPANGIRI WU UKUTHANDIZIRA KUONJEZERA CHITHUNZITHUNZI CHA TIZILOMBO TA TOXOPLASMA



PAKALI PANO, NDI UPANGIRI WATSOPANO WA MAJINI WU, TIMATHA KUPHUNZIRA NDI KUFUFUZA ZA MAJINI WA MWAMSANGA.

MUZONSEZI, ZINTHU ZOPATSA CHIDWI ZA TIZILOMBO TI ZIKUPEZEKA



TOXOPLASMA NDI TIZILOMBO TOPAMBANA KWAMBIRI. KOMA, KUSIYANA NDI TIZILOMBO TOYAMBITSA MALUNGO, TIZILOMBO TA TOXOPLASMA TI MAPAMBANA BWINOBWINO OPANDA KUPHA ANTHU AMBIRI

ANTHU AMATHA KUKHALA NDI TIZILOMBO TI KWA ZAKA ZAMBIRI OSADZIWA




IZI ZIKHOZA KUTHEKA BWANJIZ KAWIRIKAWIRI, TIZILOMBO TOYAMBITSA TOXOPLASMOSIS TI TIMAPHEDWA NDI CHITETEZO CHA MTHUPI NDIPO ZOTSATIRA ZA KULIMBANAKU NDI ZIMENE ZIMAYAMBITSA ZIZINDIKILO ZAMBIRI ZAMATENDA WA




KOMA TIZILOMBO TA TOXOPLASMA TIMATHA KUBISALA OSATI KULIMBANA NDIZINTHU. TIKANGOTITENGA, TIMAPEZA NJIRA ZODABWITSA ZOFUNIRA KUKHALA NDI MOYO

TIKALOWA M'THUPI, TIZILOMBO TI TIMAZEMBA POLOWA MKATI MWA TIZIGAWO TA TING'ONOTING'ONO TA M'THUPI MWATHU



TIZIGAWO TATHU TI TIMAKHALA MALO ABWINO KWA TIZILOMBO TI KUTI TISAMAONEKE NDI CHITETEZO CHA MTHUPI MWATHU. NDI KUBISALA KWA TIZILOMBO TI KU CHITETEZO CHATHU CHA M'THUPI, THUPI LIMAPITILIZA KUGWIRA NTCHITO ZAKE, MWINI THUPI OSADZIWA KALIKONSE



TIZIGAWO TA MTHUPI TAMU UBONGO, MASO NDI MINYEWA, ZONSE ZIKHOZA KUKHALA MALO ABWINO OBISALIRAPO, KOMA TIZILOMBO TI TILI NDI KUTHEKERA KOLOWA MU TIZIGAWO TA M'THUPI MWATHU TOSIYANASIYANA KOMANSO MITUNDU YA NYAMA YOSIYANASIYANA



NGAKHALE TIZILOMBO TI TIMATHA KUPANGA USHASHA KU CHITETEZO CHATHU, CHITETEZO CHA MTHUPI CHIMAKHALA CHIKUGWIRABE NTCHITO KUTI TIZILOMBO TI TISAONONGE


NGATI CHITETEZO CHASOKONEKERA, TIZILOMBO TI TIMAKHALA TILIBE CHIFUKWA CHENICHENI CHOTI TIZIBISALANSO NDIPO TIMATULUKA, KUONONGA THUPI NDI KUYAMBITSA MATENDA OOPSA OMWE AMAFUNIKA MANKHWALA KUTI ACHIZIDWE

ZOBISIKA ZOMWE ZILI MKATI MWA  
TIZILOMBO TI ZIKHOZA KUTSEGULA  
MAKOMO OSANGOCHIZIRA MATENDA  
A TOXOPLASMOSIS OKHA AYI  
KOMANSO MATENDA ENA

TIKUPEZA MAYANKHO  
OTHANDIZA POPHUNZIRA  
ZIWALO ZINA  
ZOSIYANASIYANA ZA  
TIZILOMBO TI



KACHIWALO KAMODZI  
KODABWITSA NDI KACHILENDO  
KA TIZILOMBO TI NDI  
KOTCHEDWA APICOPLAST



KACHIWALO KA KAMAONEKA  
MODABWITSA NDIPO KALI NDI  
MBIRI YACHILENDO NDI  
YOPATSA CHIDWI

ZIKUONEKA KUTI KACHIWALO KA  
APICOPLAST KALI NDI ZINTHU  
ZOFANANA NDI MA CHLOROPLAST-  
MBALI IMODZI YA ZIGAWO ZA ZOMERA  
ZOMWE ZIMAGWIRA NTCHITO  
POPANGA ZAKUDYA KUDZERA MU  
DZUWA. CHIWALO CHIMENE  
CHIMAPANGITSA CHOMERA  
KUKHALA CHOBIRIWIRA



NDIZOTHEKA KALEKALELO KUTI MAKOLO  
A TIZILOMBO TI AMAKHALA MOYO  
WOFANANIRAPO NDI ZOMERA



MKATIKATI MWA KUSINTHA, TIZILOMBO TI  
TINATENGA NJIRA YOSIYANA, KUSINTHA  
NKUKHALA TOXOPLASMA

NGAKHALE KALI NDI MBILI YAKALEKALE, KACHIWALO KA APICOPLAST NDIKOFUNIKA KUMOYO WA TIZILOMBO TI. NDIKOFUNIKA KUTI TIKHALE NDI MOYO POGWIRA NTCHITO YOFUNIKIRA MU KAKULIDWE, KUDZIKONZA NDI KUCHULUKANA

KAFUKUFUKU WAPEZA KUTI TIKHOZA KUONONGA APICOPLAST YA TOXOPLASMA NDI MANKHWALA A MBEU, KUONONGA TIZILOMBO TI NGATI UDZU KU MUNDA



POMVETSETSA MMENE APICOPLAST IMAGWIRIRA NTCHITO, KOMANSO MMENE TINGAYIONNGERE, ZINGAKHALE ZOTHANDIZA



TIKHOZA KUGWIRITSA NTCHITO UTHENGAWU POTHANA NDI TIZILOMBO TINANSO, NDI MA APICOPLAST AKEAKE. TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDA A MALUNGO TIKHOZANSO KUPHEDWA MOTERE POTI TILI NDI KACHIWALO KA APICOPLAST KAMENIKA.



IZI NDI ZOWME ZIMAPANGITSA MALO OGWIRIRA NTCHITO A WELLCOME CENTRE FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY KUKHALA OSANGALATSA

AKATSWIRI AUKADAULO WA TIZILOMBO TOSIYANASIYANA AMATHA KUGWIRIRA NTCHITO LIMODZI POPEZA NJIRA NDI UPANGIRI WATSOPANO WOFANANA WOMWE UNGAGWIRITSIDWE NTCHITO POGONJETA TIZILOMBO TI



KUYAMBIRA MALUNGO  
MPAKANA KAODZERA KENAKA  
TOXOPLASMOSIS, WELCOME  
CENTRE NDI MALO  
OGAWANILANAKO NZERU  
PAKATI PA NTHITO ZATHU  
ZOSIYANASIYANA. NDI  
MALONSO AMGWIRIZANO  
AZAUPANGIRI WA ZA TIZILOMBO  
TI PA DZIKO LONSE LAPANSI.



TILI KUZUKUTA MOZAMA  
TIZILOMBO TOYAMBITSA MATENDAWA  
NDIPO TIKUMVETSETSA ZA TINTHU  
TING'ONTING'ONO TOSAONEKA NDI  
MASO TI KUPOSA KALE

KOMABE, MAFUNSO AMBIRI  
OFUNIKIRA SANAYANKHIDWEBE  
MOTI NTHAWI ZINA KUPEZA  
ZATSOPANO ZA TIZILOMBO TI  
KUMABWERETSA MAFUNSO  
ENA AMBIRINSO.

TIKUFUNANSO TITAFALITSA UTHENGA WA TIZILOMBO TIMENE TI,  
PODZIWIWISA ANTHU KUOPSA KWAKE NDIKUTI ANTHU AMVETSETSE ZA  
SAYANSI YA TIZILOMBO NGATI TOXOPLASMA



NDEUKUTI BWANJI,  
USIYA KUTHAMANGITSA  
MAKOSWEZ?



MREW?



KOMABE, USIYE  
KUNDISIYIRA MAKOSWE  
AKUFA NGATI MPHATSO

**WELLCOME CENTER FOR INTEGRATIVE PARASITOLOGY**  
IMAPEZEKELA KU SUKULU YA UKACHENJEDWE YA GLASGOW. NTCHITO  
YATHU YAIKULU NDI KUFUFUZA ZA MMENE TIZILOMBO TOYAMBITSA  
MATENDA OSIYANASIYANA TIMAGWILIRA NTCHITO MTHUPI MWA MUNTHU  
KUTI TIPEZE MANKHWALA NDI NJIRA ZOTIGONJETSERA

KUTI MUDZIWE ZAMBIRI ZA NTCHITO YATHU, ONANI TSAMBA LA INTANETI  
**[WWW.GLA.AC.UK/WCIP](http://WWW.GLA.AC.UK/WCIP)**

KAPENA CHEZANI NAFE PA TSAMBA LA MCHEZO LA TWITTER  
**[@WCIPGLASGOW](https://twitter.com/WCIPGLASGOW)**

TIKUTHOKOZA DR LILACH SHEINER, DR VICKIE CURTIS, NDI ONSE AMENE  
ANATENGAPO GAWO POWELENGA BUKULI KUTI LIMVEKE BWINO

ZAMBIRI ZA OLEMBA BUKU LA NTHABWALI MUNGAZIPEZE PA:

[WWW.EDWARDROSS.CO.UK](http://WWW.EDWARDROSS.CO.UK)

[WWW.JPJHALL.NET](http://WWW.JPJHALL.NET)



University  
of Glasgow

Wellcome Centre  
for Integrative  
Parasitology



TOXOPLASMA! TIZIOMBO TODABWITSA TIMENE TIMAPEZA MOKHALA  
MU AMPHAKA, ANTHU, MAKOSWE NDI NYAMA ZINA. PAFUPI FUPI  
THEKA LA ANTHU ONSE PA DZIKO LAPANSI ALI NDI MATENDA WA  
KOMA SAMAPHA MWACHISAWAWA

DZIWANI ZA TIZIOMBO TOSANGALATSA TI, MMENE TIMAFALITSIRA  
MATENDA NDI CHIFUKWA CHOMWE AKADAULO A ZASAYANSI  
AMAKHULUPILIRA KUTI TIKHOZA KUPANGITSA MWINI THUPI ASINTHE  
ZOCHITIKA

MBALI IMODZI YA NKHANI ZA TIZIOMBO ZOMWE INAWINA MPHOTO



University  
of Glasgow

Wellcome Centre  
for Integrative  
Parasitology

